



Chithunzithunzi
(The Image)



TIMVERENI

Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana

Kulimbikitsa Ufulu wa Ana Kudzera M maphunziro, Zaluso ndi Njira
zofalitsira Mauthenga



TIMVERENI

Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana

**Kulimbikitsa Ufulu wa Ana Kudzera
M'maphunziro, Zaluso ndi Njira
zofalitsira Mauthenga**

Chithunzithunzi

Kabukuka ndi kamodzi mwa maphunziro a TIMVERENI, Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana. TIMVERENI ndi maphunziro olimbikitsa ufulu wa ana kudzera m'maphunziro, zaluso ndi njira zofalitsira mauthenga. Mabukuwa analembedwa mu chaka cha 2011 ngati mbali imodzi ya pulojekiti ya IPEC/ILO ndi chithandizo chochokera ku boma la Italy.

IPEC/ILO ikulimbikitsa kuti mabukuwa angathe kuyikidwa mu zilankhulo zosiyanasiyana komanso kusindikizidwanso kuti ntchito yothetsa nkhanza kwa ana ipite patsogolo. Ngati mwathanthauzira bukuli mu chinenero china kapena kusinthako mbali ina ya mabukuwa, kumbukirani kunena komwe mwatenga uthengawo ndiponso mutumizireko a ILO/IPEC mabukuwa kapena mbali yomwe mwasintha.

TIMVERENI – Lekani Nkhaza. Kulimbikitsa ufulu wa ana kudzera m'maphunziro, zaluso ndi njira zina zofalitsira mauthenga, Ntchito Yolimbana ndi Mchitidwe Olemba Ntchito Ana pa dziko lonse, International Programme on the Elimination of Child Labour (IPEC),

International Labour Organisation (ILO),
Geneva, 2011.

ISBN N. 92-2-113 240-4

Mungathe kudziwa zambiri za TIMVERENI kuchokera ku:

International Programme on the Elimination of Child Labour (IPEC)
International Labour Organisation (ILO)

4, Route des Morillons, CH-1211 Geneva 22, Switzerland
Telephone: +41 22 799 77 47
Fax: +41 22 799 81 81
Email: childlabour@ilo.org
Web site: www.ilo.org/scream

Cholinga: Kupanga chithuzithuzi cha mwana wolembedwa ntchito. Kuzindikira za momwe mwana wolembedwa ntchito amakhalira, pa dziko lonse lapansi.



Phindu: Kuthandiza kumvetsa za mchitidwe wogwiritsa ntchito ana komanso kuzindikira zowawa zomwe anawo amakumana nazo chifukwa cha khalidwe limeneli. Kuyamba kuganizira za momwe anthu angasinthire pa nkhaniyi.

Nthawi

Maphunziro anayi kapena awiri ophatikizana.



Chilimbikitso

Ngati munapanga kale phunziro la “Kupanga Zithunzi” (**Collage**), ndiye kuti gulu lanu likuzindikira kuti ndizosavuta kuti anthu akhale osalabadira pa nkhani ya khalidwe lolemba ntchito ana aang'ono ndi kumakhala ngati kuti vutoli kulibe. Pa nthawiyi munaona kuti pakufunika yankho pa nkhaniyi. Tsopano aliyense anazindikira kuti vutoli lilipo ngakhale kuti palibe amene akudziwa maonekedwe a vutoli pakuti nkhaniyi siyipezeka kwambiri mu ma nyuzipepala ngakhaleenso mu magazini. Funso ndi lakuti, “kodi vutoli limaoneka bwanji?” Choncho phunziroli lithandiza kutambasula maonekedwe a khalidwe lolemba ntchito ana aang'ono.

Cholinga cha gawo ili ndi kuthandiza gulu kuti liganizire za maonekedwe a khalidwe lolemba ntchito ana aang'ono. Ngati vutoli lilipo m'dera lanu, mungathe kutenga gulu lanu kuti likakumane ndi ana okhudzidwawo.

Chidziwitso

Ngati mukufuna kuchita maphunzirowa mu m'ndandanda woyenera, tikukupemphani kuti muyambe ndi phunziro la “Kupanga zithunzi” musayambe phunziro ili. Phunziro limenelo likugwiritsanso ntchito zithunzi ndipo zingayende bwino mutayambira phunziro limenelo. Zingathandizenso ngati gulu lanu likudziwa bwino zokhudza kukula kwa vuto la kugwiritsa ntchito ana aang'ono monga zafotokedwa mu phunziro la “Zofunika kudziwa” komanso ngati munachitako maphunziro a momwe mungakopere anthu.



Mwina ena mu gulu lanu anakumanako ndi mavutowa kapenanso akudziwa ana ena amene angathe kukufotokozerani okha zomwe anakumana nazo. Ngati kudera lanu kulibe amene anaonako kapena kumva za vutoli, gwiritsani ntchito chithunzi cha ana akugwira ntchito yoposa msinkhu wawo kuti anthu a mu gulu lanu aone okha ndipo amvetsetse za vutoli.

Zimenezi zikuthandizani kuti muganizire bwino za mavuto okhudzana ndi kulemba ntchito ana aang'ono. Cholinga chake ndi kuti muyambe kudziwa ndi kumvetsa za mwana wogwiritsidwa ntchito ndi kuyamba kulingalira zimenezi pa inu nokha ngati munthu. Gawoli lidzayambitsa achinyamata kuti akhale okhudzidwa ndi nkhanayi mpaka mwina kukhumudwa kumene ndi zimene ana amakumana nazo. Ndi zokayikitsa ngati angapezeke osakhudzidwa ndi nkhanayi kumapeto kwa phunziroli.

Gawo lachiwiri la zochita lithandiza kufotokozerana mozama za kumene mwana wogwiritsidwa ntchito amakhala ndi kugwirako ntchito. Gawoli likuyala mbiri komanso tsogolo la mwanayo. Pomaliza, likuwunikanso nkhanayi ya kusintha ndi momwezinthu zingasinthire.

Mwina mu gulu lanu muli achinyamata omwe anagwirako ntchito zothandiza okalamba kapena ana ovutika ndi mabungwe monga a **Red Cross** kapena **Red Crescent**. Ntchito zonsezi zili ndi zolinga zofana zomwe ndi kuthandiza anthu omwe ali pa chiopsezo cha moyo wawo, oponderezedwa, kusalidwa kapenanso kuzunzidwa kwa mitundu yosiyanasiyana.

Zonsezi ndi zosonyeza kuti aliyense ali ndi udindo wothandiza kuti zinthu zisinthe pa dziko.

Mu gawoli muphunziranso luso lokambirana zinthu mopatsana mpata kuti aliyense anene maganizo ke pa mutu uliwonse wa nkhanayi ndi cholinga chakuti gulu limange mfundo imodzi. Njirayi ndi yothandiza kuti aliyense amasuke kunena za kumtima kwake mopanda mantha, makamaka zinthu zobisika. Njirayi idzathandizanso kuti achinyamata akhazikike pa malingaliro awo othetsa mchitidwe ogwiritsa ntchito ana.

Zofunikira

- Chithunzi cha mwana wogwiritsidwa ntchito zoposa msinkhu wake.
- Chipinda chomwe gulu lanu lingagwiliremo ntchito. Ngati gulu lanu ndi lalikulu kwambiri, ligaweni ndi kukhala ndi timagulu tingapo kenako maguluwa akhale ndi malo awo mu chipindacho.
- Malo pa khoma kuti mupachikepo chithunzcha mwana wogwiritsidwa ntchito yoposa msinkhu wake.
- Pepala komanso zolembera ngati pensulo kuti muzilembera mfundo zomwe mwakambirana.
- Bolodi kapena mapepala akuluakulu, ngati angapezeke.



Kukonzekera

Pokonzekeraochitika mu phunziroli, sankhani chithunzi kapena zithunzi za ana ogwira ntchito ndipo onetsetsani kuti muli nazo zokwanira kuti aliyense angathe kuona (ngati simungathe kupeza zithunzi zokwanira, musadandaule, mungathe kugwiritsa chithunzi chimodzi). Mungathenso kusankha pa zithunzi zomwe zili mu kaphukusi ka maphunzirowa za ana omwe akugwira ntchito m'malo osiyanasiyana.

Mungathenso kupeza zithunzi zina pogwiritsa ntchito njira ngati izi:

- Ngati muli ndi makina a kompyutala kapena mgwirizano wa makompyutala (Internet), website ya **IPEC** (www.ilo.org/public/english/standards/ipecc/index.htm) ili ndi zithunzi zingapo za ana ogwira ntchito. Sankhani chithunzi chomwe chingakusangalatseni ndi kukwaniritsa zofuna zanu ndi kuchisindikiza pa pepala kapena kuchisunga mu kompyutala yanu kenako ndi kuchikonzanso kuti chioneke bwino ndi kompyutala yanu. Ndi zosangalatsa ngati mungakwanitse kutsukitsa chithunzi chanu kuti chioneke ndi makaka onse, koma ngati ndizosatheka, palibe kanthu. Sindikizanu zithunzi ambiri kuti zikwaniregulu lonse.





Chidziwitso

Bungwela IPEC linakonza m'ndandanda wa zithunzi za maphunzirowa zomwe mungazipeze mu **CD-ROM** yomwe ikupezeka mu buku la "Malamulo ndi mapangano a dziko lonse, ndi zithunzi za ana olembedwa ntchito". Mungathe kuzipezanso zithunzizi ndi **CD-ROM** ku maofesi a **IPEC**. Keyala ya **IPEC** ikupezeka kumapeto a bukuli.



- Zithunzi zina mungathe kuzipeza ku bungwe la ILO komanso mabungwe ena monga **UNICEF, One World, UNESCO** kapena **Christian Aid**.

Posankha zithunzizi muyenera kuganizira zinthu monga izi:

- Ganizirani nkhani yakufanana pakati pa amuna ndi akazi (**gender**), zaka komanso miyambo ndi zikhulupiriro za anthu a mu gulu lanu. Zimenezi zikuthandizani kusankha zithunzi zoyenera gulu lanu monga ngati ndi kofunika kupeza chithunzi cha m'nyamata kapena m'tsikana, wa ku Africa, Asia kapena mayiko ena. Kodi mukufuna kupeza chithunzi chowonetsa komwe khalidweli lafika poyipitsitsa kwambiri? Choncho mungathe kupeza zithunzi zosiyanasiyana poganizira zinthu zomwe mukufuna kuwonetsa.
- Sankhani zithunzi zowoneka bwino kuti achinyamatawa athe kuzindikira bwino zomwe zikuwonetsedwa ndi kukhala okhudzidwa ndi uthenga wa mu zithunzizo poyerekeza ndi zomwe iwo amaona pa moyo wao ndiponso momwe akukhalira m'deralawo.
- Onetsetsani kuti zipangizo monga mapensulo komanso mapepala ndi okwanira kuti aliyense athe kulemba zonse zofunikira mu phunziroli. Pa nthawi ya zokambirana, gwiritsani ntchito bolodi kapena mapepala akuluakulu ngati mungathe kupeza zimenezi. Ngati simungathe kuzipeza zimenezi, afunsi ena a mu gulu lanu ngati angakwanitse kupeza zipangizosi kunyumba kapena kukapemphakumalo ngati masitolo ndi maofesi.
- Ngati aliyense kutenga mbali, zidzathandiza kupanga umwini ndi kubweretsa chidwi pa zochitika za gulu. Komanso anthu ofunsiwa kuti athandize adzakhala ndi chidwi kuti adziweza zomwe zikuchitika.

Kuyamba

Gawo loyamba la phunziroli ndi lopanga chithunzithunzi cha mwana wogwiritsidwa ntchito yoposa msinkhu wake kuchokera ku zithunzi zosiyanasiyana. Ichi ndi chiyambi chabwino pothandiza gulu kuti liyambe kupanga chithunzithunzi cha maonekedwe a khalidwe logwiritsa ntchito ana aang'ono m'maganizo awo. Akamaliza kupanga zithunzizo ayenera kuwonetsa amnzawo a magulu ena ndi kuyankha mafunso komanso kutenga mbali pa zokambirana.



Pali njira ziwiri zomwe mungatsate mu zochita za gawo ili. Mungathe kugwiritsa ntchito chithunzi chimodzi mu magulu onse kapena kugwiritsa ntchito zithunzi zosiyanana ndi cholinga chakuti achinyamatawa azindikire kuti vutoli limaoneka mosiyanasiyana. Njirayomwe mungasankhe idzatengera momwe inu mwaonera.

Chithunzithunzi

Potsata kukula kwa gulu lanu, mungathe kuwaika achinyamatawa mu gulu limodzi kapena kugawa magulu angapo koma osapitilira magulu anayi kapena asanu. Onetsetsani kuti ali zithunzi zokwanira magulu onse kapena kuti gulu lililonse likutha kuona chithunzi.

Kukonza gulu

Chifukwa chomwe ndi kwabwino kugwira ntchitoyi m'magulu ndi chakuti aliyense amakhala omasuka opanda mantha. Mwina zingathe kukhala zovuta kupanga zithunzithunzi zimenezi aliyense payekhapayekha koma kukhala m'magulu a anthu angapo kumathandiza kuchotsa mantha.



Gawo loyamba la zochita: Kukonza chithunzithunzi cha mwana wogwiritsidwa ntchito

Phunziro limodzi la magawo awiri kapena maphunziro awiri apadera

Gulu lililonse liyendetse chithunzi pakati pawo kuti aliyense achione. Ngati palibe zithunzi zokwanira magulu onse, yendetsani chithunzi chimodzi kuti aliyense akhale ndi mwayi wochionera pafupi, mukatero muchipachike pa khoma kuti aliyense adzitha kuchiona ndi kulingalira pa zomwe akuwona pa nthawi a zochitikazi. Ngati zithunzi zinali zokwanira bwino, aliyense akamaliza kuona, chithunzi chiyikidwe pakati pa gulupomwe aliyense angathe kumachiona.

Yenderani magulu onse ndi kuwalimbikitsa kuti adzionetsetsa zithunzizo ndi kulingalira mozama pa nkhani yaana oponderezedwa. Afotokozereni kuti atambasule maganizo awo momasuka.

Gawo limeneli lili ndi ndimeziwiri:

Kuyala mfundo zofunikira



Ndime yoyamba ndiyothandiza aliyense kuti aganize za kuti kodi mwanayo ndi ndani ndipo amakhala malo otani kapena amagwira ntchito potani. Guli lingathe kudzifunsa mafunso angapo. Alembeni mafunsowa penapake kuti aliyense adzifunse yekha. Mungathenso kuwalemba mafunsowa pa pepala ndi kusiyako mipata yoti angathe kumaikamo mayankho. Musakonze mafunso ambiri koma asiyireni mpata wakuti ngathe kuwonjezerapo mafunso awo. Kuwapatsa mpata wokonza mafunso pawokha kudzathandiza kuti akhale odzidalira poganiza.

Alimbikitseni kuti ayambe kumanga chithunzithunzi cha nkhanayi potsatira mafunso ngati awa:

- Kodi mwanayo ndi wamkazi kapena wa mamuna?
- Nanga mukuganiza kuti ali ndizaka zingati?
- Kodi amachokera dziko liti?
- Nanga ndi chifukwa chiyani iye wavala zovala zimenezi kapena ndi chifukwa chiyani wanyamula zipangizo zimenezi?
- Kodi imeneyi ndi nthawi yanji?

- Kodi mwanayu amagwira ntchito m'malo otani?
- Kodi kumeneku ndi kumudzi kapena kutawuni?

Mwina maguluena angakondekuyamba kukonza chithunzithunzichi ngati nthano kapena maganizo chabe. Ena angakonde kukhazikitsa chithunzichi m'maganizo awo kapenanso kuyamba kujambula zithunzi zina pa chithunzichi zosonyeza zomwe iwo akuganiza. Njira iliyonse ndi yololedwa. Alimbikitseni powalankhula nthawi yonse pamene akuchita zimenezi kuti chidwi chawo chisachepe.

Akamaliza kuyankha mafunso oyambawa ndipo ndi inu mwakhutitsidwa momwe iwo akuchitira mu ndime imeneyi, pitirizani ndi mafunso okhudza moyo wake wa mwanayo komanso ayambe kuganizira mozama pa nkhani ya mwanayu:

- Kodi dzinalake ndi ndani?
- Kodi wagwira ntchitoyi nthawi yayitali bwanji?
- Kodi ali ndi makolo, abale kapena ziweto?
- Nanga iyeyu ndi osauka kapena olemera?
- Ndi chifukwa chiyani iye akugwira ntchito?
- Kodi ntchito imene akugwira ikutengera kuti iye ndi wamamuna kapena wamkazi? Kodi mwanayu akuwoneka kuti wamenyedwa, kapena wosowa zinthu, wogwiritsidwa ntchito za chiwerewere kapena iye ndi wosamalidwa bwino?
- Kodi amnzake kapena adani ake ndi ndani, ku ntchito kapena kumudzi?
- Kodi mwanayu angakonde kupanga chiyani m'malo mogwiritsidwa ntchito?
- mwanayu angakonde kupanga chiyani m'malo mogwiritsidwa ntchito?
- Kodi mwanayu ali ndi maloto ena pa moyo wake oposa zomwe akupanga tsopano? Kodi iye akulakalaka atadzapanga chiyani mu moyo wake m'tsogolo?
- Kodi mwanayu ali ndi chuma kapena katundu aliyense odzipezera yekha?
- Anamupeza bwanji katunduyu kapena chumacho?
- Nanga zabwino kapena zoipitsitsa zomwe angakumbukire pa moyo wake ndi ziti?

Ndi mafunso amenewa mukuthandiza gulu lanu kuti liganize mozama komanso mwaluso. Mwina angathe kudabwa poyamba kuti "Ife tingadziwe bwanji maina awo a ana amenewa? Mwina amalankhula chilankhulo china. Nanga tingadziwe bwanji zomwe iwo amakonda?" Komatu zindikirani kuti nkhani yonse yagona pamenepa, kuti mwanayu akungomudziwa "maonekedwe" ake.

Zowonjezera pa chithunzithunzi cha mwana



Ndi ntchito yawo tsopano kuti awonjezere zinthu zina pa chithunzithunzi cha mwanayo kuti akhale munthu weniweni, zinthu zonena za moyo wake, mbiri yake komanso banja lake. Mwina poyamba achinyamatawa angathe kumanyinyirika ndi ntchitoyi koma akamvetsetsa bwino, iwo adzatha kupanga chithunzithunzi chabwino cha anawa.

Mukamawayendera, onetsetsani ngati zonse zikuyenda bwino. Mvetserani zomwe akukambirana ndi kuwonjezerapo zina zomwe mukuganiza omanso zomwe zingawasangalatse. Adziwitseni kuti angathe kugwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana zopangira chithunzithunzi cha mwanayo. Mwachitsanzo, iwo angathe kusonyeza maonekedwe a mwanayo mu sewero la chisudzo kapena kujambula ngati chithunzi pa bolodi kapena pepala lalikulu (*flipchart*).

Musaonjezere kwambiri nthawi yololedwa (mphindi 20 ndi zokwanira). Iwo ayenera kumaliza ntchito yonseyi mu nthawi yololedwa basi ndipo ngati nthawi yakwana awuzeni kuti asiye zonse kuti muyambe ndime ina ya zokambirana.

Kuwonetsa zithunzithunzi

Magulu onse adzafuna kuti akambe za munthu yemwe iwo amuona pa chithunzi chawo. Athandizeni kuti amasuke pokambirana ndi inu komanso amnzawo za mwana yemwe iwo amuona pa chithunzi chomwe gulu lawo linakambirana.



Ngati gulu lina latulutsa chithunzithunzi mwa luso lapadera kuposa amnzawo, aloleni kuti akhale oyambilira kuwonetsa amnzawo a magulu ena. Zimenezi (ngakhale sizingaoneke nthawi onse) zidzathandiza kuchotsa mantha kapena kudzikayikira kwa magulu ena. Musalole kuti nsangulutso kapena zoseketsa ziwononge kufunika kwa uthenga womwe gulu likuwonetsa.

Ngati mukuona kuti zingathandize kuwonjezera luso la gulu, yambitsani mpikisano ndi kulonjeza mphoto kwa:

- Chithunzithunzi cha mwana wolembedwa ntchito chomwe chafotokozeredwa bwino komanso mwaluso. Aloleni maguluwa kuti agamuleokha chithunzithunzi chopambana zonse.
- Chithunzithunzi chomwe chikuwonetsa kuganiza mozama.

Lembani zizindikiro za zithunzithunzi omwe zaperekedwa pa bolodi kapena pepala lalikulu (**flipchart**).

Ngati magulu onse anagwiritsa ntchito chithunzi chofanana ndiye kuti mungathe kuyamba kumanga chithunzithunzi chimodzi pamodzi ndi gulu lonse pogwiritsa ntchito zomwe magulu onse apeleka. Athandizeni kuti amvetsetse kuti aliyense wathandiza popanga chithunzithunzichi. Tsopano chithunzichi chikukhala ngati chili ndi moyo ndipo chikutha “kupuma”, “kulankhula”, “kuseka”, “kumva kuwawa” ngakhale “kulira”.



Ndime imeneyi ndi yofunika kwambiri pothandiza kuzindikiritsa achinyamata za nkhaniyi. Tsopano akutha kumvetsa za maonekedwe a mwana wolembedwa ntchito zoposa nsinkhu wake. Akuzindikira kuti mwanayu angathe kukhala mmodzi wa iwo, kuti mwanayu ndi mmodzi wa gulu lawo, mnezawo yemwe angathe kumumvera chisoni. Tsopano akumvetsa za ululu, mavuto komanso umphawi womwe mwanayu amamva tsiku ndi tsiku. Imeneyi ndi njira yothandiza kwambiri kuti achinyamata adzitha kumvetsetsa zinthu za umunthu ndi kubweretsa kusintha mwa iwo.

Uthenga umenewu umveke bwino pa nthawi omwe mukumaliza zokambirana za mu ndime imeneyi. Gwiritsani ntchito njira zothandiza kuti achinyamatawa amvetse bwino kufunika kwa uthengawu makamaka zowakopa kuti akhale ndi umunthu pa nkhaniyi. Yang'anani m'maso mwa aliyense pa nthawi imene mukufotokoza za moyo wa mwana amene iwo akambirana mu magulu awo. Mungathe kugwiritsa ntchito manja anu kapenanso nkhope yanu posonyeza mavuto omwe mwanayu akukumana nawo. Ngakhale kuti imeneyi ndi ndime yomvetsa chisoni, zindikirani zimenezi sizachilendo chifukwa nkhani yonse yokhudza khalidwe logwiritsa ntchito ana aang'ono ndi yokhumudwitsa kumene. Siyosangalatsa. Ingathe kuvulaza ngakhale kupha ana. Ndi chachidziwikire kuti khalidweli limaononga moyo wa ana komanso kuwamana ufulu wa chibadwidwe – ufulu wokhala munthu womasuka.

Gawo lachiwiri la zochita: Kudziwa zambiri za ana olembedwa ntchito

Phunziro limodzi



Ana ogwiritsidwa ntchito amapezeka kulikonse. Alipo m'dera lanu kapena kufupi ndi kudera kwanu. Sikuti iwo amapezeka mu dziko longopeka ayi. Angathe kupezeka ngakhale ku nyumba zomwe mwayandikana nazo. Choncho gulu lanu lidziwe kuti izi sinkhambakamwa chabe kapena nthano. Tikuyenera tsopano kuyamba kuyiganizira nkhaniyi monga momwe ikuchitikira pakati pa anthu, komanso pa dziko lonse ngati mudzi umodzi.

Pamene azindikira kuti vutoli lilipodi, iwo adzaona kufunika kwake kwakuti zinthu zisinthe ndiponso kuti aliyense akhale wokhudzidwa ndi ndi mmene zinthu ziliri ndi kuyamba kulimbana ndi kuti zinthu zisinthe.

Ndime yotsatirayi ithandiza kulimbikitsa gulu lanu kupitiriza kulingalira za moyo wa mwana wogwiritsidwa ntchito monga momwe ziliri mu ndime yoyamba ya phunziro limeneli. Ndime imeneyi ndi yosangalatsa ndipo zinthu zambiri zingathe kunenedwa, zina zothandiza ndi ina zosathandiza kwenikweni. Ngakhale zili choncho, ndime imeneyi idzathandiza kuti gulu lanu limvetsetse nkhaniyi ndi kuti mwina iwo angasanduke “asilikali” obweretsa kusintha.

'Kugogodana mitu'

Kugogodana mitu ndi njira yokambirana ndi kutambasula nkhani pogwiritsa ntchito nzeru za anthu angapo mu nthawi yochepa. Aliyense amakhala ngati ali pa mpanipani makamaka chifukwa nthawi imakhala yochepa komanso malo ake opangira zokambirana amakhala osapereka mpata okhala motakasuka. Zimenezi ndi zimene zimapangitsa kuti munthu agwiritse ntchito mutu wake mwansanga ndi kutulutsa maganizo omwe ali nawo pa nthawi yomwe yaperekedwa. Choncho anthu amalankhula zakukhosi kwawo popanda kuganizira kwambiri zotsatira za zomwe akulankhula. Nthawi zambiri, njira imeneyi imathandiza kuti anthu alankhule zoona komanso zotsekulana maso. Choncho ngati njirayi yagwiritsidwa ntchito bwino, imakhala yothandiza.

Samalani pogwiritsa ntchito njirayi imeneyi kuti mupewe chisokonezo chomwe chingabwere chifukwa phokoso lobwera ndi anthu omwe angafune kuti maganizo awo amveke ndi kuganiziridwa. Ngati simunakonzekere bwino, mungathe kukhala pa mavuto aakulu. Njira yabwino yoyendetsera zokambiranazi ndi kuti mukonzekere bwino ndi kudziwa zomwe zikuchitika. Lembani mfundo zonse zofunika ndiponso onetsetsani kuti zokambirana zikuyenda mofulumira. Aliyense adziganiza mofulumira mosapatsidwa nthawi yambiri kenako anene maganizo ake.



Onetsetsani kuti magulu akhale monga zinaliri mu gawo loyamba la zochita ndipo mupereke chithunzi chomwe anagwiritsa ntchito poyambapo.

Ntchito za m'magulu

Onaninso zithunzithunzi zomwe zinapangidwa gawo loyamba, gwiritsani ntchito mphindi khumi. Ndi kofunika ugwiritsa ntchito maina omwe magulu anapereka ku zithunzithunzi zawo kuti mulimbikitse cholinga cha phunziro limeneli kuti achinyamatawa akhale ndi chithunzi chenicheni cha nkhanza zomwe ana ogwiritsidwa ntchito amakumana nazo. Makamaka inuyo ngati mlangizi, uyenera kugwiritsa ntchito maina amenewa ndipo gulu lanu lidzachita imodzimodzi. Zimenezi zidzalimbikitsa ubale weniweni pakati pa inu ndi mwana wa mu chithunzithunzi chomwe chapangidwa.

Zotsatira za kusintha kwa zinthu

Ndime yotsatira ya gawo limeneli ndi kuganizira zomwe zingachitike ndikukhudza moyo wa ana olembedwa ntchito. Makamaka funsani gulu lanu kuti liganizire zomwe zachitika kwanu, mu Africa komanso dziko lonse lapansi ndi uwunika zomwe zakhudza moyo wa ana omwe ali mu zithunzi aja.

Gwiritsani ntchito njira ija yokambirana zinthu poganiza mofulumira yomwe tafotokozera kale m'mwambamu. Cholinga ndi chakuti anthu aganizire zomwe zachitika dziko lonse zomwe zakhudza miyoyo ya ana omwe amalembedwa ntchito zoposa nsinkhu wao, zabwino kapena zoipa.

Choncho mu ndime yotsatirayi, auzeni a gulu lanu kuti ayerekeze kuti chithunzi chomwe amagwiritsa ntchito chinajambulidwa zaka ziwiri kapena zitatu za m'mbuyomu. Akatero aganizire mwansanga zinthu ziwiri zazikulu zomwe zachitika kuchokera nthawi imeneyi kufikira lero ndi kuwona ngati zimenezi zasintha moyo wa mwana ali pa chithunzi uja. Mungathe kupanga zimenezi potsata njira izi:



- Auzeni kuti alembe papepala zonse zomwe zachitika pa nthawi.
- Mungathenso kuwauza kuti azingotchula zomwe zachitika, funsani munthu m'modzi kuti akhale kutsogolo ndi kulemba zimenezi pa bolodi kapena pa malo pena paliponse pomwe mwakonza. Mwina njira imeneyi ingakhale yosangalatsa kwambiri komanso yobweretsa chidwi pa zokambiranazi.

Fotokozerani gulu kuti zochitikazi zingathe kukhala china chilichonse monga masewera olimbitsa thupi, nkondo ya pa chiweniweni, kunyanyala ntchito, ziwonetsero, kubwera kwa alendo otchuka, zivomerezi kapena kusefukira kwa madzi, ngakhale imfa anthu otchuka. Nkhani iliyonse ndi yovomerezeka.

Pangitsani zokambirana kukhala zosangalatsa popeleka nthawi yochepa pakati pa mphindi 5 kapena 10. Aliyense atengepo mbali, mungathenso kuwonjezera zosangalatsa popeleka zitsanzo zina za zinthu zomwe zachitika pa nthawiyo zomwe mwina achinyamatawa sangaziganizire msanga monga nkondo, kusintha kwa boma, misonkhano yaikulu ya atsogoleri a pa dzikolonsendi zina zotere.



Mukaona kuti maganizo ayamba kuchepa kapena kutha, tsekani ndime imeneyi ndi kuyamba kuona mndandanda wa zomwe zalembedwa. Kambiranani ndi kuwunika ngati pa zomwe zalembedwazi pali zinthu zomwe zabweretsa kusintha pa moyo wa ana olembedwa ntchito zoposa msinkhu wao (omwe ali mu zithunzi aja).

Funsani mafunso monga:

- Kodi pali zomwe zabweretsa kusintha kwabwino kapena koipa, kapena zosalabadira pa miyoyo ya ana olembedwa ntchito zoposa msinkhu wao? Kusintha kwake ndi kotani?
- Kodi iwo akuganiza kuti mwana ali pa chithunzi uja akupanga chiyani tsopano pakuti waonjezera zaka zitatu pa msinkhu wake?
- Kodi mwanayu wasintha mwa njira ina iliyonse mu zaka zitatu zimenezi? Kodi mwanayu ali moyo?
- Kodi iye akugwirabe ntchito?
- Kodi akusewera ndi amnzake kapena ndi abale ake kunyumba?



Limbikitsani kukambirana pa mafunsowa ndipo athandizeni pamene ndi pofunika kutero. Popitilira ndi ndimeyi, gulu lidzayamba kuzindikira kuti vuto logwiritsa ntchito ana aang'ono lafika pachimake ndipo likufunika mayankho msanga ngakhale kuti ndi pa nthawi ino pa zonse zomwe zikuchitika pa dziko lapansi ndi zochepa zomwe zibweretsa kusintha pa moyo wa ana oponderezedwawa. Iwo akungogwirabe ntchito yowawa ndi chiyembekezo chakuti mwina zinthu zidzawayendera bwino koma mwatsoka nthawi zambiri maloto awo amalephera kukwaniritsidwa. Tsopano gulu lanu likuyenera kuzindikira kufunika kwa usintha pa moyo wa ana onse oponderezedwawa.

Ngati mwaona kuti mwamaliza zonse za mu ndimeyi, mungathe kupitiriza ndi ndime yotsatirayi.

**Kumenya nkhondo
yosintha zinthu**

Ili ndi gawo lomaliza la zochita mu phunziroli. Monga mwachitira m'mbuyomu, gwiritsani ntchito njira yomvera maganizo a anthu mwansanga yomwe tafotokozera kale. Cholinga cha ndime yomalizayi ndi kuganizira zinthu zomwe zingachitike ndi kubweretsa kusintha pa moyo wa ana omwe mwawaona muzithunzi aja.

Afunseni mafunso monga:



- Kodi munthu kapena magulu a anthu angapange chiyani kuti moyo wa ana olembedwa ntchito usinthike?
- Kodi anthu a mu gulu lanu angapange chiyani kuti moyo wa anawa usinthe?
- Kodi kusintha kwenikweni kumabwera bwanji pa dziko lapansi?
- Kodi kusintha pakati pa anthu a msinkhu umodzi ngati a mu gulu lanu kumabwera bwanji?
- Kodi anthu a mu gulu lanu akuganiza kuti kusintha pa moyo wa anawa ndi kofunika?
- Chifukwa chiyani?

Monga mwachitira kale, limbikitsani kukambirana momasuka mu mphindi 5 kapena 10, komatsopano inuyo mutsogolere zokambiranazi komanso muzilemba pa bolodi kapena pa flipchart. Chitani changu pofunsa mafunso ndipo onetsetsani kuti mayankho akubwera msanga mosalola kuti munthu ayambe kuganizira ngati yankho lake ndi lovomerezeka kapena ayi. Zimenezi zidzathandiza kuti anthu, makamaka achinyamatawa, alankhuleza mu maganizo awo enieni.

Mukaona zizindikiro za kutopa, tsekani zokambiranazi. Tsenderani zonse ndi kusonkhanitsa zonse zomwe gulu likuganiza pa nthawiyo.

Zoyenera kuchita ndi zoyenera kupewa

- Alimbikitseni anthu mugulu lanu kuti aganize mozama komanso ndi masomphenya popanga chithunzithunzi cha mwana wogwiritsidwa ntchito. Mwina ena angathe kumachita zamasewera ndi kupeputsa ntchito. Amenewa adzachita manyazi poona amnzawo amagulu ena akulimbikira. Zimenezi zidzapangitsa kuti nawonso ayambe kulimbikira.
- Pasakhale kusankhana chifukwa chakuti mwina ana ena a mu gulu lanu ali m'gulu la ana ogwiritsidwa ntchito kapena kuwasala ana ena chifukwa cha zifukwa zina. Mwachitsanzo, popeleka zochita, pewani kuika anyamata mu gulu lokambirana za chithunzi cha ana ogwira ntchito "zofunika mphamvu" kapena zomwe anthu amaona kuti ndi zachimuna, ndi kuika atsikana kuti akambirane za chithunzi cha mwana ogwira ntchito za pakhomu. Kuterondiki kulakwitsa zinthu.
- Limbikitsani kuti pasakhale kusiyanitsa ntchito za anyamata ndi atsikana chifukwa ndi zotheka kuti anyamata ndi atsikana agwiritsidwe ntchito zofanana monga momwe zimachitikira ku mayiko ena kuti anyamata amakakamizidwa kuchita za uhule.
- Musapereke mafunso ambiri kwa gulu lanu koma alimbikitseni kuti apeze mafunso pawokha. Zikatero iwo angathe kutulutsa mafunso a nzeru zozama zomwe zili zabwino chifukwa zidzaonetsa kuti ali ndi chidwi komanso akutenga nawombali.
- Alimbikitseni onse kuti atenge nawombali mu zochitikazi.
- Pa nthawi "yogogodana mitu" gulu likhale lomasuka kuchita ka mpungwepungwe pang'ono ndi cholinga chakuti anthu athe kutambasula maganizo awo mosamangika komanso mwachangu.
- Bweretsani nsangulutso monga nthabwala pa nthawiyi kuti zokambiranazi zipepuke ngakhale kuti zimakhala zomvetsa chisoni kwa achinyamatawa.
- Onetsetsani kuti zokambiranazi zichitike mwachangu. Njira imeneyi imagwira bwino ntchito ngati anthu apanikizidwa kuti anene maganizo awo. Funsani mafunso afupiafupi komanso a changu kwa aliyense mugulu makamaka anthu omwe akuwoneka amanyazi.
- Musalole kuti zokambiranazi mulowe chisawawa chobwera chifukwa cholimbirana kuti aliyense amveke kapena kupezerapo mwayi ongonenapo zinthu zopanda nzeru.
- Ngakhale kuti njira yokambiranayi imalimbikitsa kuti aliyense anene za kukhosi kwake momasuka, sibwino kuti ena atengerepo mwayi wopeputsa nkhani ya mchitidwe wogwiritsachito ana aang'ono. Chonchosamalani ndi kutsogolera bwino zokambiranazi.



- Onetsetsani kuti zokambiranazi sizikutenga nthawi yoposa muyeso woyenera chifukwa anthu angathe kutopa mwansanga ngakhale kutaya chidwi chawo pa nkhami.
- Ganiziraninso kusiyana kwa chikhalidwe cha anthu mu gulu lanu. Onetsetsani kuti ngakhale achinyamata ndi osiyana, aliyense apatsidwe mpata kupereka maganizo ake komanso kupanga nawo zina zonse zomwe gululikuchita.
- Gwiritsani bwino ntchito nthawi yokambirana zomwe zachitika polimbikitsa kulankhula momasuka komanso mwaufulu.

Kukambirana komaliza

Phunziro limodzi



Ngati mukuyamba ndime imeneyi mutangomaliza kumene “kugogodana mitu”, gwiritsani ntchito gawo limeneli ngati nthawi yoziziritsira mitu komanso kubwezeretsa mphamvu m'thupi. Yambani ndi nkhami zina zongochiza ngakhale zosakhudzana ndi mchitidwe wogwiritsa ntchito ana aang'ono. Ndi chachidziwikire kuti nkhami zambiri zomwe zingakambidwe zingatse kukhala za kulemba nchito ana aang'ono.

Pa nthawi imene maganizo awo akhazikika, mungathe kuyamba kukambirana nkhami yayikulu ya funso lakuti “kodi kusintha kungabwere bwanji mu dziko?” Afotokozereni kuti kusintha kumayamba ndi anthu a m'mudzi ngakhale dziko lonse omwe ali ndi chilakolako cha kusintha. Chilakolako chimenechi ndi chomwe chimayambitsa kukonzekera kuchita zinthu, kenako ndi kuchita zinthu zothandiza kuti zinthu zisinthe. Kusintha kumabwera pamene anthu ambiri akufuna kusinthako pa nthawi imodzi. Kusintha kumabwera pamene iwo akakamiza atsogoleri awo a m'mudzi, andale, boma lawo ngakhale mabungwe a m'dera lawo ndiponso dziko lonse kuti achitepo kanthu kuti zinthu zisinthe.

Kusintha kumatheka popeza chithandizo kuchokera ku mabungwe a m'mudzi, oimira anthu a pa ntchito, mabungwe a za chifundo ndi ena otere. Zonse zimagana nthawi, chilimbikitso, kudzipereka komanso kukhala okonzeka kuchitapo kanthu.

Kusintha kulikonse kuli ndi chiyambi. Kungathe kuyamba ndi achinyamata monga momwe zimalembedwera mu mabuku a mbiri yakale. Choncho achinyamata ayenera kudziwa kuti mu umodzi muli mphamvu. Nkhondo yolimbana ndi mchitidwe wogwiritsa ntchito ana inayamba kale koma achinyamata akuyenera kuthandiza potenga nawo mbali polimbana ndi khalidweli. Chithandizo chawo ndi chofunika kwambiri makamaka chifukwa nkhanayi ikuwakhudza ngati a msinkhu umodzi ndi ana olembedwa ntchito.

Tsekani zokambiranazi ndi uthenga wa chiyembekezo chifukwa tsopano chiwerengero cha anthu ozindikira za maonekedwe a mwana wogwiritsidwa ntchito zoposa msinkhu wake chakwera chifukwa chakuti gulu lanu lachita nawo phunziroli. Iwo athandiza kuti chithunzi cha mwana wogwiritsidwa ntchito chikhale chenicheni “cha moyo” ndipo tsopano iwo adzakumbukira chithunzithunzi chimenechi m'moyo kwa nthawi yaitali. Ngati inu ndi gulu lanu mupitiriza maphunziro ena a mu mndandanda wa maphunzirowa, chithunzithunzichi chidzakhala chotambasuka bwino. Choncho alimbikitseni kuti akhale ndi chidwi chopititsa patsogolo zomwe adziwazi komanso kukweza chilakolako choona zomwe zingachitike kutsogolo.

Kuunika momwe ntchito yayendera ndi kuchita kalondolondo

Kuphatikiza pa zotsatira za phunziroli, pali zizindikiro zina zokhudza umunthu zomwe zithandize pounika phindu pa momwe phunziroli layendera.

Zotsatira zowoneka ndi maso pa gawo loyamba a phunziroli ndi zithunzithunzi zomwe magulu onse anakonza. Chizindikiro cha mlingo wakupambana mu ndimeyi ndi kuzama kwa zithunzithunzi komanso uthenga womwe umapezeka pa zithunzizo. Zimenezi zikuwonetsa momwe gulu “linamulandirira” mwanayo. Chithunzithunzi chofotokozeredwa bwino komanso chowonetsedwa mwaluso chikusonyeza chidwi chomwe achinyamatawa anali nacho pa nkhanayi.

Mu gawo lachiwiri la zochita simunatuluke china chilichonse chapadera. Chizindikiro chakupambana mu ndimeyi ndi mlingo wa chidwi komanso kujijirika kwa achinyamatawa pa zokambirana makamaka mu ndime “yogogodana mitu”. Muona kuti zomwe zikuwunikidwa kwambiri ndi momwe achinyamatawa anachitira gawo lopanga zithunzithunzi za mwana wolembedwa ntchito.



Zimenezi ndiye zizindikiro za kupambana kwa phunziro limeneli kwa achinyamataa mugulu lanu.

Phunziro limeneli ikulumikiza nkhani ya kuzindikira ndi ya kukhala okhudzidwa ndi umunthu pa vuto logwiritsa ntchito ana aang'ono. Phunziroli linakonzedwa kuti lilimbikitse kuzindikira kuti kulemba ntchito ana aang'ono ndi vuto komanso kuzindikira kuti vutoli limakhudza ana aang'onoang'ono omwe ndi anthu enien omwe amayenda, amalankhula komanso kumva kuwawa. Phunziroli ndi la m'phamvu ndipo ingathe kukhala losayiwalika kwa gulu lanu. M'madera ambiri, anthu amaganiza kuti kuponderezedwa kapena kuphwanyidwa kwa ufulu sikungawachitikire, kuti ndi zinthu zachilendo kwa wo. Nthawi zambiri timaganiza kuti zinthu zochitika kwina sizingatikhudze. Phunziro limeneli ndi lothandiza kusintha kuganiza kwa mtundu umenewu ndi kuyamba kuzindikira kuti vutoli lilipo monga mwaonera mu zithunzi zomwe mwakambirana mu phunziroli.

Tsopano achinyamatawa ayamba kufuna kuthandiza bungwe la IPEC pa ntchito zake chifukwa ayamba kukhala okhudzidwa ndi amnzawo omwe akuona zovuta chifukwa chogwira ntchito zoposa msinkhu wao. Chithunzi chomwe aona mu phunziroli chayamba kukhala munthu weniweni yemwe ndi m'modzi mwa anthu olozeka m'gulu lawo.

Ngati mwakhutitsidwa kuti mwamaliza phunziroli, mungathe kuyamba phunziro lina. Zingakhale zothandiza kuyamba phunziro lomwe mukagwiritse ntchito zithunzithunzi zomwe magulu anu anakonza, za "mwana" yemwetsopano akudziwika ndi gulu lonse. Mwachitsanzo, phunziro la "Masewero a Zochitika Zenizeni" lingathe kupereka mpata (pogwiritsa ntchito masewero) kuti mupitirize kumudziwa bwino "mwana" amene mwayamba kumudziwa mu phunziro mukumalizali.



Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana

ILO

International programme on the
Elimination of Child Labour (IPEC)

ILO/ IPEC Malawi Project
Mantino Complex
Behind Bizonowaty filling station
PO BOX 30135
Lilongwe

Tel: (+265)-0- 1 770 388/ 199/155

www.ilo.org/ipecc

ISBN 92-2-113240-4

